LIVING ON THE EDGE™

MPINGO WAMPHAMVU

ZOPOSA

Mbiri ya Wophunzira

LIVING ON THE EDGE™

ZOKHUDZA UTUMIKI WA LIVING ON THE EDGE

Utumiki wa Living on the Edge ulipo pothandiza Akhristu kuti adzikhala monga Akhristu. Utumikiwu unayambitsidwa mu 1995 ngati utumiki wa pawailesi wa a Chip Ingram, yemwe ndi m'busa komanso wa zolembalemba. Pakali pano, Mulungu anakulitsa utumikiwu n'kukhala utumiki wa ophunzira dziko lonse lapansi. Utumiki wa Living on the Edge umapereka ziphunzitso komanso zipangizo kwa Akhristu onse padziko lapansi kuti ziwathandize kukhala ophunzira a Yesu Okhwima.

MPINGO WAMPHAMVU
ZOPOSA

Zam'katimu

Phunziro 1 ..... Tsamba 4

Chiyambi

Phunziro 2 ..... Tsamba 16

Kodi Mulungu Akufuna Chiyani kwa Ine?

Phunziro 3 ..... Tsamba 22

Kodi Ndingapeze Bwanji Zabwino za Mulungu M'moyo Wanga?

Phunziro 4 ..... Tsamba 28

Kodi Cholinga cha Mulungu pa Moyo Wanga ndi Chiyani?

Phunziro 5 ..... Tsamba 36

Kodi Ndingakhale Bwanji Mogwirizana ndi Anthu Ena?

Phunziro 6 ..... Tsamba 42

Ndingathane Bwanji ndi Zoipa Zolunjika pa Ine?

Phunziro 7 ..... Tsamba 48

Chochita chotsatira ndi chiti?

LIVING ON THE EDGE™

MPINGO WAMPHAMVU

Z O P O S A

Chiyambi

PHUNZIRO 1

1. Kodi Tili Pano Lero Chifukwa Chiyani?

A. Kuti TILEMEKEZE Mulungu.

> Lemekezani AMBUYE pamodzi ndi ine; tiyeni tikweze dzina lake pamodzi.
>
> MASALIMO 34:3

B. Kuti TISUNTHIRE chifupi ndi Mulungu.

> Tiyeni tisunthire chifupi ndi Mulungu moona mtima ndi chitsimikizo chachikulu chimene chikhulupiliro chimabweretsa...
>
> AHEBERI 10:22

C. Kuti TIPEZE njira za mu Buku Lopatulika zosinthira anthu kuti akhale ophunzira.

> Chifukwa chake mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu.
>
> MATEYU 28:19-20

Ntchito: Zokambirana

1. Khalani m'magulu a anthu a pakati pa 3 ndi 5, ndipo aliyense adzifotokoze mwachidule. Kodi m'kuyembekezera zotani mu nthawi yathu limodzi?
2. Kodi muli ndi masomphenya otani pa ana anu (kapena ana anu am'tsogolo)?

2. Masomphenya a Mulungu pa Mpingo Wanu

A. Kholo lirilonse liri ndi **MASOMPHENYA** pa ana ake.

B. Mulungu wathu wakumwamba ali ndi masomphenya pa aliyense mwa **ANA** ake.

C. Masomphenya a Mulungu ndi kupanga ana ake kukhala monga **YESU**. (Mateyu 5:48, Aroma 8:29, Aefeso 4:13)

D. Malingaliro a Mulungu posintha anthu kuti akhale ophunzira ndi **MPINGO**. (Mateyu 5:13-16)

"Chofunikira chachikulu mumpingo ndi kuti Akhristu adzikhaladi monga Akhristu." - CHIP INGRAM

E. FUNSO: Kodi **MPINGO** **WABWINO** umaoneka bwanji?

3. Zizindikiro Zitatu za Mpingo Wabwino

A. Anthu otaika AMABWERA KWA KHRISTU.

NTCHITO YAIKULU

"Ndipo Yesu anadza nalankhula nawo, nanena, Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine Kumwamba ndi pa dziko lapansi. Chifukwa chake mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndi ili pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira chimaliziro cha nthawi ya pansi pano."

MATEYU 28:18-20

B. Anthu opezeka AMAKULA M'KAKHWIMIDWE .

LAMULO LALIKULU

"Udzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse ndi moyo wako wonse ndi nzeru zako zonse.' Ili ndilo lamulo lalikulu ndi loyamba. Ndipo lachiwiri lolingana nalo ndi ili: 'Udzikonda mnzako monga udzikonda iwe mwini.' Pa malamulo awa awiri mpokolowekapo chilamulo chonse ndi aneneri."

MATEYU 22:37-40

C. Anthu okonzekera KUKWANIRITSA ZOSOWA m'dera.

CHIFUNDO CHACHIKULU

" Pomwepo Mfumuyo idzanena kwa iwo a kudzanja lake lamanja, Idzani kuno inu odalitsika a Atate wanga, lowani mu Ufumu wokonzedwera kwa inu pa chikhazikiro chake cha dziko lapansi: pakuti ndinali ndi njala, ndipo munandipatsa Ine kudya; ndinali ndi ludzu, ndipo munandimwetsa Ine; ndinali mlendo, ndipo munachereza Ine; wamaliseche Ine, ndipo munandiveka; ndinadwala, ndipo munadza kucheza ndi Ine; ndinali m'nyumba yandende, ndipo munadza kwa Ine. Pomwepo olungama adzamyankha Iye kuti, Ambuye, tinakuonani Inu liti wanjala, ndi kukudyetsani? Kapena waludzu, ndi kukumwetsani? Ndipo tinaona Inu liti mlendo, ndi kukucherezani? Kapena wamaliseche, ndi kukuvekani? Ndipo tinakuonani Inu liti wodwala, kapena m'nyumba yandende, ndipo tinadza kwa Inu? Ndipo Mfumuyo idzayankha nidzati kwa iwo, Indetu ndinena kwa inu, Chifukwa munachitira ichi mmodzi wa abale anga, ngakhale ang'onong'ono awa, munandichitira ichi Ine."

MATEYU 25:34-40

Mpingo wanu ukapanga zinthu zitatu izi, ndiye kuti ndi MPINGO WAMPHAMVU ZOPOSA!

4. Zomwe Mipingo Yabwino Ikufunikira Kuti Ithe Kusintha Anthu N'kukhala Ophunzira

A. . Mpingo uliwonse ukufunika kukhala ndi CHITHUNZITHUNZI CHABWINO cha kukhala wophunzira.

B. Mpingo uliwonse ukufunika atsogoleri amene POYAMBA ndi ophunzira ndipo KACHIWIRI ndi atsogoleri.

"Mpingo udzadzuka ndi kugwa chifukwa cha utsogoleri wa uzimu wa abusa ake komanso mphamvu za ophunzira ake."
- DENNIS BARIL

C. Mpingo uliwonse ukufunika MBIRI ndi NDONDOMEKO kuti usinthe anthu kuti akhale ophunzira.

5. Mbiri ya wophunzira: Aroma 12

1 Chifukwa chake ndikupemphani inu, abale, mwa zifundo za Mulungu, kuti mupereke matupi anu nsembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera.

2 Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire chimene chili chifuno cha Mulungu, chabwino, ndi chokondweretsa, ndi changwiro.

3 Pakuti ndi chisomo chapatsidwa kwa ine, ndiuza munthu aliyense wa inu, kuti asadziyese koposa kumene ayenera kudziyesa; koma aganize modziletsa yekha, monga Mulungu anagawira kwa munthu aliyense muyeso wa chikhulupiriro. 4 Pakuti monga m'thupi limodzi tili nazo ziwalo zambiri, ndipo ziwalo zonsezo sizili nayo ntchito imodzimodzi, 5 chomwecho ife, ndife ambiri, tili thupi limodzi mwa Khristu, ndi ziwalo zinzake, wina ndi wina. 6 Ndipo pokhala ife ndi mphatso zosiyana, monga mwa chisomo chopatsidwa kwa ife, kapena mphatso yakunenera, tinenere monga mwa muyeso wa chikhulupiriro; 7 kapena yakutumikira, tidzipereke ku utumiki uwu; kapena iye wakuphunzitsa, kukuphunzitsako; 8 kapena iye wakudandaulira, kukudandaulirako; wakugawira achite ndi mtima woona; iye wakuweruza, aweruze ndi changu; iye wakuchita chifundo, achite ndi kukondwa mtima.

9 Chikondano chikhale chopanda chinyengo. Dana nacho choipa; gwirizana
nacho chabwino. 10 M'chikondano cha anzanu wina ndi mnzake mukondane
ndi chikondi chenicheni; mutsogolerane ndi kuchitira wina mnzake ulemu.
11 Musakhale aulesi m'machitidwe anu; khalani achangu mumzimu,
tumikirani Ambuye. 12 Kondwerani m'chiyembekezo, pirirani m'masautso;
limbikani chilimbikire m'kupemphera. 13 Patsani zosowa oyera mtima;
cherezani aulendo.

14 Dalitsani iwo akuzunza inu; dalitsani, musawatemberere.

15 Kondwani nao iwo akukondwera; lirani nao akulira. 16 Mukhale ndi mtima
umodzi wina ndi mnzake. Musasamalire zinthu zazikulu, koma phatikanani
nao odzichepetsa. Musadziyesere anzeru mwa inu nokha. 17 Musabwezere
munthu aliyense choipa chosinthana ndi choipa. Ganiziranitu zinthu za
ulemu pamaso pa anthu onse. 18 Ngati nkutheka, monga momwe mukhoza,
khalani ndi mtendere ndi anthu onse. 19 Musabwezere choipa, okondedwa,
koma patukani pamkwiyo; pakuti kwalembedwa: "Kubwezera kuli kwanga,
Ine ndidzabwezera," ati Ambuye. 20 "Koma ngati mdani wako akumva njala,
umdyetse, ngati akumva ludzu, ummwetse; pakuti pakutero udzaunjika
makala a moto pamutu pake." 21 Musagonje kwa choipa, koma ndi chabwino
gonjetsani choipa.

AROMA 12:1-21

A. Maubale akuluakulu asanu opezeka pa Aroma 12:

MULUNGU (vesi 1)

DZIKO LAPANSI (vesi 2)

INUYO (vesi 3 mpaka 8)

OKHULUPILIRA (vesi 14 mpaka 21)

OSAKHULUPILIRA (vesi 14 mpaka 21)

B. Momwe WOPHUNZIRA amakhalira potsatira Aroma 12:

Mulungu → KUPEREKA moyo wanga

Dziko lapansi → KULEKANA ndi mfundo za m'dziko lapansi

Inuyo → KUDZIUNIKA moona mtima

Okhulupilira → KUTUMIKIRA m'chikondi

Osakhulupilira → Kubwezera chabwino ku choipa motsogozedwa ndi MZIMU WOYERA .

C. Musaphonye izi: Kukhala wophunzira WENIWENI:

- Kumatengera chisomo, osati ntchito zathu
- Kwagona pa maubale, osati zomwe timayankhulana ndi ena
- Kwagona pochita, osati kulingalira chabe
- Kumayezedwa, osati wosaoneka bwinobwino

6. Vuto

A. Ndikosatheka KUPEREKA chimene MULIBE. Tikuyenera KUKHALA omwe tikufuna anthu athu kuti AKHALE.

B. Mulungu ayenera agwire ntchito MWAKUYA mwa ife asanagwire ntchito YAMPHAMVU kudzera mwa ife.

Kudzipereka ku Utsogoleri

- Ndikudzipereka kukhala WOPHUNZIRA wa Yesu ndisanakhale MTSOGOLERI pa ntchito ya Yesu.

Ntchito - Kulingalira Payekhapayekha komanso Kukambirana

1. Kulingalira: Kuti mumvetsetse, dziunikeni nokha komanso mpingo wanu pogwiritsa ntchito mulingo wa 1 mpaka 10 pa chizindikiro chilichonse cha wophunzira:

> "Ndinakufunani ndi mtima wanga wonse; ndisasokere kusiyana nao malamulo anu."
>
> (MASALIMO 119:10)

Ndipereka moyo wanga kwa Mulungu

	Gawo la Moyo Wanu Lofunika Kukula					Gawo la Moyo Wanu Lomwe Mukuchita Bwino				
INU	1	2	3	4	5	6	7	8	9	10
MPINGO	1	2	3	4	5	6	7	8	9	10

Kulekana ndi Mfundo za M'dziko Lapansi

	Gawo la Moyo Wanu Lofunika Kukula					Gawo la Moyo Wanu Lomwe Mukuchita Bwino				
INU	1	2	3	4	5	6	7	8	9	10
MPINGO	1	2	3	4	5	6	7	8	9	10

Kulekana ndi Mfundo za M'dziko Lapansi

	Gawo la Moyo Wanu Lofunika Kukula					Gawo la Moyo Wanu Lomwe Mukuchita Bwino				
INU	1	2	3	4	5	6	7	8	9	10
MPINGO	1	2	3	4	5	6	7	8	9	10

Kutumikira Okhulupilira Ena Mwachikondi

	Gawo la Moyo Wanu Lofunika Kukula					Gawo la Moyo Wanu Lomwe Mukuchita Bwino				
INU	1	2	3	4	5	6	7	8	9	10
MPINGO	1	2	3	4	5	6	7	8	9	10

Kubwezera Chabwino ku Choipa Motsogozedwa ndi Mzimu Woyera

	Gawo la Moyo Wanu Lofunika Kukula					Gawo la Moyo Wanu Lomwe Mukuchita Bwino				
INU	1	2	3	4	5	6	7	8	9	10
MPINGO	1	2	3	4	5	6	7	8	9	10

2. Kukambirana: Khalani m'magulu a anthu a pakati pa 3 ndi 5, ndipo potengera momwe mwadziunikira pamwambapa, fotokozani gawo limodzi la moyo WANU lomwe mukuchita bwino ndi gawo limodzi la moyo WANU lomwe simukuchita bwino.

3. Sankhani munthu m'modzi kapena awiri kuti apemphere kuti Mulungu ativumbulire tanthauzo la kukhala mtsogoleri mu Ufumu Wake.

LIVING ON THE EDGE™

MPINGO WAMPHAMVU

ZOPOSA

Kodi Mulungu Akufuna Chiyani kwa Ine?

PHUNZIRO 2

Kodi Mulungu akufuna chiyani kwa ine?

Chizindikiro choyamba cha wophunzira wa pa Aroma 12 chikukhudza ubale wathu ndi **MULUNGU**.

1. Momwe Tingamupatsire Mulungu Zimene Iye Akufuna

> Chifukwa chake ndikupemphani inu, abale, mwa zifundo za Mulungu, kuti mupereke matupi anu ngati nsembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera.
>
> AROMA 12:2

A. **Lamulo:** "____PEREKAN____ matupi anu ngati nsembe ya moyo"

B. **Chilimbikitso:** "____CHIFUNDO____ cha Mulungu"

C. **Chifukwa chake:** "____KUPEMBEDZA____ koyenera ."

2. Kudzipereka ndi Kupembedza Muchoona

A. Mulungu akufuna INU NONSE ! (Eksodo 20:3, Mateyu 6:33)

> Ufumu wa Kumwamba uli wofanana ndi chuma chobisika m'munda; chimene munthu anachipeza, nachibisa; ndipo m'kuchikonda kwake achoka, nagulitsa zonse ali nazo, nagula munda umenewu. Ndiponso Ufumu wa Kumwamba uli wofanana ndi munthu wa malonda, wakufuna ngale zabwino: ndipo m'mene anaipeza ngale imodzi ya mtengo wapatali, anapita, nagulitsa zonse anali nazo, naigula imeneyo."
>
> MATEYU 13:44-46

B. **Vuto:** timatenga kudzipereka ngati chinthu CHOIPA komanso ngati KUGONJETSEDWA .

C. **Chilungamo chake:** Kudzipereka ndi NJIRA imene madalitso abwino ndi aakulu a Mulungu amadzera. (MASALIMO 84:11)

D. Kudzipereka ndi CHIGANIZO komanso NDONDOMEKO. Ndi chisankho chimene chimabweretsa khalidwe.

> Pamenepo ananena kwa iwo, “Moyo wanga uli wozingidwa ndi chisoni cha kufika nacho kuimfa; khalani pano muchezere pamodzi ndi Ine.” Ndipo anamuka patsogolo pang’ono, nagwa nkhope yake pansi, napemphera, nati, “Atate ngati nkutheka, chikho ichi chindipitirire Ine; koma si monga ndifuna Ine, koma Inu.”
>
> MATEYU 26:38-39

E. Timamupatsa Mulungu CHILICHONSE pomupatsa Iye CHINTHU CHOTSATIRA.

> Ndipo anati, “Tengatu mwana wako, wamwamuna wayekhayo, Isake amene ukondana naye, numuke ku dziko la Moriya; numpereke iye kumeneko nsembe yopsereza pa limodzi la mapiri lomwe ndidzakuuza iwe.”
>
> GENESESI 22:2

Kudzipereka ku Utsogoleri

- Ndikutsimikiza KUDZIPEREKA zonse zimene ndi ili ndi zonse zimene ndi ili nazo kwa Mulungu.

Ntchito - Zokambirana

1. Khalani m'magulu a anthu a pakati pa 3 ndi 5. Kodi mukuganiza kuti n'chifukwa chiyani Akhristu ambiri samakhala moyo wodzipereka?

2. Kodi "Isake" wanu ndi chiyani? Kodi chinthu chotsatira chimene Mulungu akukupemphani kuti mumupatse ndi chiyani?

3. Sankhani munthu mmodzi kapena awiri kuti apemphere kuti Mulungu akupatseni mphamvu yoti mupereke "Isake" wanu kwa iye.

LIVING ON THE EDGE™

MPINGO WAMPHAMVU

ZOPOSA

Kodi Ndingapeze Bwanji Zabwino za Mulungu M'moyo Wanga?

PHUNZIRO 3

Kodi Ndingapeze Bwanji Zabwino za Mulungu M'moyo Wanga?

Chizindikiro chachiwiri cha wophunzira wa pa Aroma 12 chikukhudza ubale wathu ndi **DZIKO LAPANSI.**

1. Momwe Mungapezere Zabwino za Mulungu pa Moyo Wanu

> Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano, koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire chimene chili chifuno cha Mulungu, chabwino, ndi chokondweretsa, ndi changwiro.
>
> AROMA 12:2

A. Kodi ndi chifukwa chiyani pali ZIGANIZO za chipulumutso zambiri koma OPHUNZIRA odzipereka ochepa?

B. **Lamulo loletsa:** “Musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano....”

Kumasulira kwake: Musiye kulola kuti kakhalidwe ndi kaganizidwe kanu kadzitsanzira ZOCHITIKA ndi zilakolako za m’dziko lino lapansi.

Kugwiritsa ntchito kwake: Tikuyenera kukhala OLEKANA ndi mfundo za m’dziko lapansi.

C. **Lamulo la zoyenera kuchita:** “... khalani osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu.”

Kumasulira kwake: Lorani Mulungu kuti akusintheni kwathunthu m’kaganizidwe ka mkati mwanu ndi khalidwe lanu lakunja pogwirizana naye moona mtima nthawi ndi nthawi komanso ndi dongosolo la kusintha kotsogozedwa ndi Mzimu.

Kugwiritsa ntchito kwake: Tikuyenera kupangidwa ndi MAWU, osati DZIKO lapansi..

2. Kulekana ndi Mfundo za M'dziko Lapansi

> Musakonde dziko lapansi, kapena za m'dziko lapansi. Ngati wina akonda dziko lapansi, chikondi cha Atate sichili mwa iye. Pakuti chilichonse cha m'dziko lapansi, chilakolako cha thupi ndi chilakolako cha maso, matamandidwe a moyo, sizichokera kwa Atate, koma kudziko lapansi. Ndipo dziko lapansi lipita, ndi chilakolako chake; koma iye amene achita chifuniro cha Mulungu akhala kunthawi yonse.
>
> 1 YOHANE 2:15-17

Chidule chake: Dongosolo la dziko lapansi limafuna kutikopa ife kuti tichoke ku chikondi cha Khristu kudzera mu ZOSANGALATSA THUPI, CHUMA, ndi MAUDINDO.

3. Ngodya za Kusintha Kaganizidwe Kanu

A. Ndi ndondomeko **YOPITILIRA** . (Akolose 3:1-4)

B. Ndi **NKHONDO** . (2 Akorinto 10:4-5)

C. Ndi ntchito **YAUZIMU** yogwiridwa ndi Mzimu Woyera. (Aroma 8:5-6)

4. Njira Zotsata Posintha Kaganizidwe Kanu

A. **MVETSERANI** Mawu a Mulungu (Aroma 10:17)

B. **WERENGANI** Mawu a Mulungu (Chibvumbulutso 1:3)

C. **ZUKUTANI** Mawu a Mulungu (2 Timoteo 2:15)

D. **LOWEZANI** Mawu a Mulungu (Masalimo 119:9,11)

E. **LINGALIRANI** Mawu a Mulungu (Yoswa 1:8)

"Tikufunika kukhala anthu a m'Buku Lopatulika: Osati anthu ongodziwa chabe zomwe Buku Lopatulikalo likunena, koma anthu amene amakhala moyo wa mu Buku Lopatulika komanso wotsogozedwa ndi Buku Lopatulika, anthu amene ali odzadzidwa ndi Mawu a Mulungu, anthu amene amakhala komanso kupuma Mawuwo,"- - N.T. WRIGHT

Kudzipereka ku Utsogoleri

- **Ndikutsimikiza kuti ndidzikhala ndi nthawi yolumikizana ndi Mulungu tsiku lililonse kuti ndisinthidwe ndi Mawu**

Ake pofuna kutetezeka ku MAYESERO **a dziko lapansi.**

Ntchito nawo- Kulingalira Payekhapayekha komanso Kukambirana

1. Kodi ndi zovuta zanji zimene zimakulepheretsani kukhala ndi nthawi ya Mawu a Mulungu?

_____

_____

_____

2. Khalani m'magulu a anthu a pakati pa 3 ndi 5, ndipo sankhani munthu mmodzi kuti awerenge mawu a pa Afilipi 4:8 mokweza:

> Pomaliza, abale ndi alongo, kalikonse komwe kali koona, kalikonse komwe kali kolemekezeka, kalikonse komwe kali kolondora, kalikonse komwe kali koyera, kalikonse komwe kali kosangalatsa, kalikonse komwe kali kosiliritsa—ngati kalikonso kali kopambana ndi kotamandika—ganizirani za zimenezo. AFILIPI 4:8

3. Perekani mwayi kwa munthu wina aliyense kuti afotokoze china chake cha m'moyo kapena muutumiki wawo chomwe chili choona, cholemkezeka, cholondora, choyera, chosangalatsa, chosiliritsa, chopambana, kapena chotamandika.

LIVING ON THE EDGE™

MPINGO WAMPHAMVU

ZOPOSA

Kodi Cholinga cha Mulungu pa Moyo Wanga ndi Chiyani?

PHUNZIRO 4

Kodi Cholinga cha Mulungu pa Moyo Wanga ndi Chotani?

Chizindikiro chachitatu cha wophunzira wa pa Aroma 12 chimakhudza ubale wathu ndi **IFE ENI AKE.**

1. Mafunso Atatu Odziwika Kwambiri

A. Kodi ndine ndani? (CHONDIZINDIKIRITSA)

B. Kodi ndi ili mbali iti? (CHITETEZO CHANGA)

C. Kodi ndikuyenera kuchita chiyani? (KUFUNIKIRA KWANGA)

2. Chondizindikiritsa Changa

> Pakuti ndi chisomo chapatsidwa kwa ine, ndiuza munthu aliyense wa inu, kuti asadziyese koposa kumene ayenera kudziyesa; koma aganize modziletsa yekha, monga Mulungu anagawira kwa munthu aliyense muyeso wa chikhulupiriro.
>
> AROMA 12:3

Lamulo: ganizani MOLONDOLA zokhudza inu mwini.

Kodi ndine ndani? Ndine wosankhidwa, woyera, mwana wa Mulungu, ndi wolandira chisomo Chake (Aefeso 1:4-8).

3. Chitetezo Changa

> Pakuti monga m'thupi limodzi tili nazo ziwalo zambiri, ndipo ziwalo zonsezo sizili nayo ntchito imodzimodzi; chomwecho ife, ndife ambiri, tili thupi limodzi mwa Khristu, ndi ziwalo zinzake, wina ndi wina.
>
> AROMA 12:4-5

Lamulo: Kukwaniritsa UDINDO wanga wopatsidwa ndi Mulungu.

Kodi ndi ili mbali iti? Mubanja la Mulungu.

4. Kufunikira Kwanga

> Ndipo pokhala ife ndi mphatso zosiyana, monga mwa chisomo chopatsidwa kwa ife, kapena mphatso yakunenera, tinenere monga mwa muyeso wa chikhulupiriro; kapena yakutumikira, tidzipereke ku utumiki uwu; kapena iye wakuphunzitsa, kukuphunzitsako; kapena iye wakudandaulira, kukudandaulirako; wakugawira achite ndi mtima woona; iye wakuweruza, aweruze ndi changu; iye wakuchita chifundo, achite ndi kukondwa mtima.
>
> AROMA 12: 6-8

Lamulo: Zindikirani ndi KUGWIRITSA NTCHITO mphatso zanga zauzimu.

Kodi ndikuyenera kuchita chiyani? Tumikiranani m'chikondi (Tikambirana mutu uwu pa phunziro lotsatira).

5. Monga M'tsogoleri

A. CHONDIZINDIKIRTSA CHANGA: Muli olandiridwa MOPANDA MALIRE mwachisomo cha Mulungu. Kotero, mumakhala komanso kutumikira CHIFUKWA CHA kuvomereza Kwake, osati kutumikira KUTI akuvomerezeni.

> Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiriro, ndipo ichi chosachokera kwa inu: chili mphatso ya Mulungu; chosachokera kuntchito, kuti asadzitamandire munthu aliyense.
>
> AEFESO 2:8-9

B. CHITETEZO CHANGA: Mulungu amakuikani pamene mukuyenera kukhala. Nthawi iliyonse yomwe MUKUDZIFANIZIRA ndi atsogoleri ena, MUMALEPHERA nthawi zonse.

> Pakuti ife ndife chipango chake, olengedwa mwa Khristu Yesu, kuchita ntchito zabwino, zimene Mulungu anazipangiratu, kuti tikayende m'menemo.
>
> AEFESO 2:10

C. KUFUNIKIRA KWANGA: Monga mtsogoleri mu mpingo; Mukuyenera **KUKONZEKERETSA** ena kuti atumikire.

> Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi ena aneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; kuti akonzere oyera mtima kuntchito ya utumiki, kumangirira thupi la Khristu.
>
> AEFESO 4; 11-12

Kudzipereka ku Utsogoleri

- Ndikutsimikiza kudalira **CHISOMO** cha Mulungu ndi **ANTHU** a Mulungu pokwaniritsa ntchito ya utumiki, chifukwa sindingathe kuchita chilichonse pandekha.

Ntchito - Kulingalira Payekhapayekha komanso Zokambirana

1. Kudziyesa pa Lingaliro la Payekhapayekha;

   Kodi ndingapititse patsogolo bwanji luso langa lokonzekeretsa ena?

   _____

   _____

   _____

   A. Potengera zomwe zili pa Aroma 12, pezani mphatso zauzimu zimene Mulungu wakupatsani:

   ○ uneneri ○ kulimbikitsa ○ kutsogolera
   ○ kutumikira ○ kupereka ○ kuonetsa chifundo
   ○ kuphunzitsa

   B. Kulingalira Payekhapayekha: Kodi ndi chiyani chikukulepheretsani kuika chidwi pa mphatso yanu yaikulu yauzimu?

   _____

   _____

   _____

C. Lingalirani ntchito yanu m'magawo akuluakulu atatu:

NDIYENERA KUCHITA (Mwayi Wolunjika pa China Chake)	NDIYENERA KUCHITA (Mwayi Wounika)	NDIKANACHITA (Mwayi Wotuma Ena)
CHOFUNIKIRA KWAMBIRI ←		→ CHOFUNIKIRA PANG'ONO

2. Kukambirana: Khalani m'magulu a anthu a pakati pa 3 ndi 4. Ndi chiyani chofunikira kwambiri chokhudza inu chomwe mwazindikira pa phunziroli?

LIVING ON THE EDGE™

MPINGO WAMPHAMVU

Z O P O S A

Kodi Ndingakhale Bwanji Mwaumodzi ndi Anthu Ena?

PHUNZIRO 5

Kodi Ndingakhale Bwanji pa Mogwirizana ndi Anthu Ena?

Chizindikiro chachinayi cha wophunzira wa pa Aroma 12 chikukhudza ubale wathu ndi **OKHULUPILIRA**.

1. Zofunika Kuchita kuti Munthu Ukule Muuzimu

A. Funso: Ndi chifukwa chiyani Akhristu abwino komanso ofikapo ambiri amakhala PAMODZIMODZI MUUZIMU?

B. Akhristu ambiri samadziika PAMALO oyenera.

C. Malo oyenera ndi pomwe pali UMODZI WENIWENI.

> Chikondano chikhale chopanda chinyengo. Dana nacho choipa; gwirizana nacho chabwino. M'chikondano cha anzanu wina ndi mnzake mukondane ndi chikondi chenicheni; mutsogolerane ndi kuchitira wina mnzake ulemu; 11musakhale aulesi m'machitidwe anu; khalani achangu mumzimu, tumikirani Ambuye; kondwerani m'chiyembekezo, pirirani m'masautso; limbikani chilimbikire m'kupemphera. Patsani zosowa oyera mtima; cherezani aulendo.
>
> AROMA 12:9-11

D. Umodzi weniweni umapezeka m M'MAGULU ANG'ONOANG'ONO.

E. Dziwani kuti: si magulu onse ang'onoang'ono omwe mumakhala UMODZI WENIWENI!

F. Umodzi weniweni umaonekera ngati TITUMIKIRA M'CHIKONDI .

G. SITINGAGWERE muumodzi weniweni; pamafunika kuti tichite kufuna komanso kukhala osunga mwambo.

2. Kodi kutumikira m'chikondi chimatanthauza chiyani?

A. Kutumikira m'chikondi kumachitika ngati:

Inu WENIWENI (Aroma 12:9),

Wapezana ndi ZOFUNA zenizeni (Aroma 12:10),

Pa ZIFUKWA zoyenera (Aroma 12:11),

Komanso M'NJIRA YOYENERA (Aroma 12:12).

B. Inu weniweni, osati YEMWE MUKUFUNA KUDZAKHALA .

Kukhala chenicheni chomwe uli – "Chikondi chathu chikhale choona mtima"

Chiyero – "Mudane ndi zoipa. Gwiritsani chomwe chili chabwino."

C. Mwakumana ndi zosowa zenizeni, osati ZONGOGANIZIRA .

Kudzipereka – "Khalani odzipereka kwa wina ndi mnzake m'chikondi"

Kudzichepetsa – "Lemekezanani wina ndi mnzake koposa momwe mumadzilemekezera."

D. Pazifukwa zolondola, osati pofuna KUSANGALATSA anthu.

Cholinga – "Musakhale osowekera khama, pitirizani kukhala olimbika muuzimu, kutumikira Mulungu."

E. M'njira yolondola, osati modalira MPHAMVU zanu.

Kudalira Kumwamba – "Khalani achimwemwe m'chiyembekezo, odekha m'nyengo zowawa, achikhulupiliro m'pemphero."

Kuika Chidwi pa Zofuna – "Gawanani ndi anthu a Mulungu omwe ali osowa. Khalani ochezeka kwa alendo."

3. Kodi inu Mukukhala Muumodzi Weniweni?

Kupatula mkazi kapena mwamuna wanu, muli ndi anthu ena m'moyo mwanu omwe ...

A. AMAKUDZIWANI ?

B. AMAKUKONDANI ?

C. AMAKUUZANI chilungamo?

D. AMAKULIMBIKITSANI ?

E. Mutha kuwaimbira foni kapena kuwaitana PAKATI pa USIKU ?

F. Omwe MUMAWATUMIKIRA ?

G. AMAKUTUMIKIRANI ?

Atsogoleri ayenera kuphunzira kulandira umodzi weniweni monga iwonso *amaonetsera* umodzi weniweni kwa ena.

Kudzipereka ku Utsogoleri

- Ndikutsimikiza kuti sindidziyang'ana za maubale **ONGOGANIZIRA CHABE** okha ayi, koma ndidzakhala muumodzi weniweni potumikira anthu ena mwachikondi.

Ntchito - Kulingalira Payekhapayekha komanso Kukambirana

1. Kulingalira: Motsatira mafunso omwe ali pa ngawo la "Kodi mukukhala muumodzi weniweni," unikani maubale anu akuluakulu—kodi mukuchita bwanji?

Gawo la Moyo Loyenera Kuchitapo Kanthu									Gawo la Moyo Lochita Bwino
1	2	3	4	5	6	7	8	9	10

2. Kulingalira: Ndi athu awiri kapena atattu ati omwe muli nawo paubale kapena ubwenzi waukulu? Ndi zinthu ziti zomwe muyenera kuchita pofuna kupititsabe patsogolo ubalewu?

_____

_____

_____

3. Sankhani munthu mmodzi kapena awiri kuti apemphererane kuti adzitha kulumikizana bwino ndi anthu ena m'maubale opatsa moyo.

LIVING ON THE EDGE™

MPINGO WAMPHAMVU

ZOPOSA

Ndingathane Bwanji ndi Zoipa Zolunjika pa Ine?

PHUNZIRO 6

Ndingathane Bwanji ndi Zoipa Zolunjika pa Ine?

Chizindikiro chachisanu cha wophunzira wa pa Arona 12 chikukhudza ubale wathu ndi iwo **OSAKHULUPILIRA**.

1. Momwe munthu ungachitire Zinthu Zosatheka

> Dalitsani iwo akuzunza inu; dalitsani, musawatemberere. Kondwani nao iwo akukondwera; lirani nao akulira. Mukhale ndi mtima umodzi wina ndi mnzake. Musasamalire zinthu zazikulu, koma phatikanani nao odzichepetsa. Musadziyesere anzeru mwa inu nokha. Musabwezere munthu aliyense choipa chosinthana ndi choipa. Ganiziranitu zinthu za ulemu pamaso pa anthu onse. Ngati nkutheka, monga momwe mukhoza, khalani ndi mtendere ndi anthu onse. Musabwezere choipa, okondedwa, koma patukani pamkwiyo; pakuti kwalembedwa, Kubwezera kuli kwanga, Ine ndidzabwezera, ati Ambuye. Koma ngati mdani wako akumva njala, umdyetse, ngati akumva ludzu, ummwetse; pakuti pakutero udzaunjika makala a moto pamutu pake. Musagonje kwa choipa, koma ndi chabwino gonjetsani choipa.
>
> AROMA 12:14-21

A. Kukhala m'Khristu wa pa Aroma 12 SIKOVUTA ... NDIKOTHEKA !

B. **Lamulo la Zoyenera Kuchita:** "Dalitsani iwo okuzunzani inu."

CHIKHULULUKIRO – "Dalitsani iwo okuzunzani inu."

KUDZIZINDIKIRITSA – "Kondwani nawo iwo akukondwera; lirani nao akulira."

KUPHATIKANA NDI ENA – "Mukhale ndi mtima umodzi wina ndi mnzake. Musasamalire zinthu zazikulu, koma phatikanani nao odzichepetsa. Musadziyesere anzeru mwa inu nokha."

C. **Lamulo Loletsa:** "Musabwezere munthu aliyense choipa chosinthana ndi choipa... Osabwezera."

Zifukwa ziwiri zasonyeza chifukwa chomwe kubwezera ndi koletsedwa.

i. Kumalanda Mulungu udindo wa OWEREUZA. "koma patukani pamkwiyo."

ii. Iyi ndi njira yabwino yobweretsera MTENDERE. "Koma ngati mdani wako akumva njala, umudyeste."

D. **Chotsatira Chozizwitsa:** UBWINO udzagonjetsa kuipa.

"Ndi chabwino gonjetsani choipa."

2. Kuchitapo Kanthu pa Choipa Motsogozedwa ndi Mzimu Woyera

A. Dziwani kuti **UKALI** uli ngati kumwa **POIZONI** kenako ndikumayembekezera munthu winayo kuti adwala naye.

B. Mankhwala a poizoni wa mkwiyo ndi **KUKHULULUKA**.

C. **YAMBANI** ulendo wa kukhululuka.



Chiganizo

Ndondomeko ya zochita

Umboni

D. FUNSO: Ndi **MPHAMVU** **YAUZIMU** yochuluka bwanji yomwe muli okonzeka kusiyana nayo chifukwa cha **UKALI** wanu?

Kudzipereka ku Utsogoleri

Ndikutsimikiza kuti ndidalira MPHAMVU YAUZIMU ya Mulungu pomwe ndikuyamba ulendo wanga wokhululuka pa choipa chilichonse cholunjika pa ine.

Ntchito - Zokambirana

1. Khalani m'magulu a anthu 3 kapena 5. Monga Yudasi anapereka Yesu m'manja mwa adani, ndi ndani yemwe anakuperekanipo inu mmanja mwa adani? Chinachitika ndi chiyani, ndipo Mulungu akukupemphani kuti mutani ndi ubale umenewu?

2. Chinthu choyamba chomwe muchite pokhululukira munthuyi ndi chiyani? Kodi pali wina wake yemwe atha kukuthandizani kuti mukwaniritse kuchita chinthucho?

LIVING ON THE EDGE™

MPINGO WAMPHAMVU

ZOPOSA

Chochita chotsatira ndi chiti?

Mwachita Bwino Kwambiri!

IZI NDIYE ZOTSATIRA:

Ulendo wanu sukuthera pano.

Tili okondwa kukuthandizani ndi zinthu zosiyanasiyana zaulele zomwe zinakonzedwa kuti zikuthandizeni kumanga Mpingo Wamphamvu Zoposa. Kuonjezera apa, tingasangalale kwambiri kumva maganizo anu! Jambulani ndi foni yanu kodi ili mmunsiyi kuti mupeze zokuthandiziranizi. Mukazipeza, ziunikeni mwachanguchangu ndi kutiuza momwe mwazionera. Tiyeni tipitirize kuphunzira ndi kukula limodzi!

LOTE.me/HIC-NY

1. Magawo Atatu a Mpingo Wamphamvu Zoposa



1) Mpingo Wabwino (Zizindikiro zitatu)

- Anthu ambiri kubwera kwa Khristu
- Anthu otembenuka kukula m'kakhwimidwe
- Anthu okonzekeretsedwa kukwanitsa kuthandizapo pa zofuna za m'dera

2) Wophunzira Wabwino (Aroma 12)

- **Kudzipereka** moyo wanga
- **Kulekana** ndi dziko lapansi
- **Kudziunika** moona mtima
- **Kutumikira** m'chikondi
- **Kubwezera chabwino ku choipa** motsogozedwa ndi Mzimu Woyera

3) Kukhala Wophunzira Wabwino

- Pamaso pa Mulungu
- M'dera
- Pa Utumiki

2. Kuchitapo Kanthu Monga Mtsogoleri wa pa Aroma 12

A. Pemphani Mulungu kuti akupatseni MASOMPHENYA ATSOPANO.

Ntchito iliyonse yopambana mu Ufumu wa Mulungu imayamba ndi pemphero! Pemphani Mulungu kuti akupatseni zikhulupiliro, nzeru, ndi kulimbamtima kwatsopano kuti muthe kukwaniritsa chifuniro chake.

B. Bweretsani kusintha ndipo pangani anthu kukhala ophunzira a pa Aroma 12 mkati ndi kunja komwe. Yambani ndi INU ENI AKE, kenako, phunzitsani ATSOGOLERI, anu ndipo malizirani ndi kufotokoza za mfundoyi MUMPINGO wanu.

INU: Mulungu akufuna kuyamba ndi kugwira ntchito yaikulu mkati mwa inu asanayambe kugwira ntchito kudzera mwa inu. Anthu anu adzatsatira chitsanzo cha inu—muyenera KUKHALA wophunzira wa pa Aroma 12 kuti naonso AKHALE choncho.

ATSOGOLERI ANU: Abusa, simungachite chilichonse panokha! Ikani chidwi pa zinthu zochepa chabe, monga Yesu amachitira. Kodi a "Petulo, Yakobo ndi Yohane" anu ndi ati? Kodi ophunzira anu "12 ndi ati?" Pogwiritsa ntchito anthu ena ochepa chabe, mumakhala mukukhazikitsa gulu la atsogoleri a pa Aroma 12. Iwo adzakuthandizani kusintha mpingo wanu kukhala Mpingo wa Mphamvu Zoposa.

MPINGO WANU: Atsogoleri anu akatsimikiza kukhala atsogoleri a pa Aroma 12, iyo ndi nthawi yoti muphunzitse mpingo wanu wonse!

Chitsimikizo cha Mtsogoleri wa pa Aroma 12

Mwachisomo cha Mulungu, ndikufuna KUKHALA munthu yemwe ndikufuna anthu anga AKHALE. Zabwino zomwe ndikulingalira ndiyamba kuzichita, kotero kuti,

- **Ndikutsimikiza kuti ndikhala wophunzira wa Yesu ndisanakhale mtsogoleri pa ntchito ya Yesu.**
- **Ndikutsimikiza kuti ndidzipereka ine ndense komanso zonse zomwe ndi ili nazo.**
- **Ndikutsimikiza kuti ndidzikhala pafupi ndi Mulungu kawirikawiri kuti ndithe kusinthika ndi Mawu Ake kusiyana ndi kugonjera mayesero a dziko lapansili.**
- **Ndikutsimikiza kuti ndidzadalira chisomo cha Mulungu ndi anthu a Mulungu kuti ndikwaniritse ntchito ya utumiki, pozindikira kuti sindingathe kuchita chilichonse pa ine ndekha.**
- **Ndikutsimikiza kuti sindidzakamba chabe za maubale enieni, ndipo ndidzakhala pa umodzi weniweni potumikira anthu ena m'chikondi.**
- **Ndikutsimikiza kuti ndidzidalira mphamvu yauzimu ya Mulungu kuti ndiyambe ulendo wokhululuka pa choipa chomwe chalunjika pa ine.**

DZINA: _____ TSIKU: _____

Munamva Bwanji Mulungu Akuyankhula?

> "Nenani, Yehova, popeza mnyamata wanu akumva."
>
> 1 SAMUELE 3:9

Lembani pemphero potsatira zomwe munamva Mulungu akukuyankhulani.